# KODI YESU NDANI?

## KABUKU KA MAYESO

### MALANGIZO KWA MUNTHU WOLEMBA MAYESO AWA

CHOYAMBA. Lembani dzina lanu, adiresi yanu ndi nambala yanu. Onetsetsani kuti muyenera kulemba dzina lanu limodzi lomwelo nthawi zonse ndiponso mosasintha malembedwe ake.

CHACHIWIRI. Yankho la funso lililonse lidzapezeka m'phunziro kapena m'ndime za m'Buku Lopatulika. Mukhoza kuyankha poyang'ana m'phunziro ndi m'Buku Lopatulika.

CHACHITATU. Mudzapeza mayankho awiri kapena opitilirapo operekedwa pa funso limodzi. Yankho limodzi likha ndilo lokhoza. Lembani nambala la yankho lokhoza pambali pake pa funsolo. Phunzirani chitsanzo chaperekedwa m'munsichi MPAKA MUTAZINDIKIRA BWINOBWINO M'MENE MUNGAYANKHIRE.

---

**CHITSANZO:**

1. Mayi wa Yesu anali:

   (1) Sara (2) Mariya (3) Elizabeti.

   Tidziwa kuti yankho lake ndilo MARIYA.
   Ili ndilo limene liri pa gawo lachiwiri
   (Yankho nambala 2) Chifukwa chake inu mulembe 2 pambali
   pa funsolo.

---

Manambala alembedwe pa malo osalembedwa pa pepala la mayeso monga pa chitsanzopo. Musalembe yankho pa malo aliwonse osalembedwa ayi kapena kudula mzere pansi pa yankho lanu ayi. Lembani nambala la yankho lanu pa malo takupatsaniwo.

CHACHINAYI. Polemba mayeso amenewa, werengani funso liri lonse mosamala, ganizirani bwino musanayankhe. Osangolemba zolota ayi. Onani pa phunziro kapena m'Buku Lopatulika ngati mwayankha bwino.

CHACHISANU. MUYENERA KUCHITA ZOTSATIRAZI POYAMBA MAYESO ANU ASANACHONGEDWE:

(a) Muyenera kuloweza ndime 'ya pamtima' ndi kuinena kwa bwenzi lanu. Ichi chidzakuthandizani kuyankha mafunso a 1 ndi 2 bwinobwino ndi mokhulupirika.

Chotsani Gawo Limeneli La Mayeso

(b) Ndikhulupirira mwawerengapo ndime zonse zimene takupatsani m'maphunzirowa.

**CHACHISANU NDI CHIMODZI.** Pamene mwatsiriza mayeso anu ONSE apindeni mosamala ndipo atumizeni kwa ife mu Inivelopi takutumiziraniyo. Adiresi yake ndi iyi: Bible Way Correspondence School, P.O. Box 292, Lilongwe-Malawi.

**CHACHISANU NDI CHIWIRI.** Onetsetsani kuti mwamata sitampa yoyenera pa Inivelopi. Ife sitidzaombola kalata yosakwanira pa mtengo wake wopositira ayi.

Pamene mwatsiliza maphunziro khumi ndi awiri abwino mudzalandira kalata yamaonekedwe abwino ya chitsimikizo (a beautiful certificate) yoyenera kuika m'feremu. Kalata ya chitsimikizoyo siikuyenerezani inu kulowa ntchito ya Chikhristu ayi. Nkofunika kwambiri kuti muphunzire maphunziro awa mwa kupemphera. Pemphani Mulungu akuthandizeni kuti muzindikire zoonadi zazikulu za Buku Lopatulika pamene muli kuphunzira mawu ake. Mulungu Mwini yekha akutsogolereni ku nzeru yake ya chipulumutso, mwa Yesu Khristu. Ngati muli Mkhristu kale, tipemphera kuti Mulungu agwiritse ntchito maphunziro awa kukulimbikitsani m'chikhulupiriro cha Chikhristu.



**CHONDE LEMBANI BWINO MAYESO ANU MUSANATUMIZE KUNO KU BIBLE WAY, P.O. Box 292, LILONGWE-MALAWI.**

Ngati mutafuna kulemba mawu owerengeka za m'mene **MAPHUNZIROWA AKUTHANDIZIRANI CHONDE LEMBANI PA TSAMBA ILI.**

## MAYESO A PHUNZIRO 12

____1. Ndaphunzira mawu a pamtima Yohane 3:16, ndipo ndanenanso kwa bwenzi langa (1) Inde., (2) Ayi.

____2. Ndawerenga mawu a Mulungu onse pa phunziro 12. (1) Inde, (2) Ayi.

____3. Pa mawu apamtima athu, timva kuti munthu angathe kukhala ndi moyo wosatha iye amene (1) Ali wophunzira kwambiri, (2) Ali wokhulupilira mwa Yesu Khristu, (3) Achita ntchito zabwino kwambiri.

____4. Mulungu ali (1) Mulungu wa anthu onse, (2) Mulungu wa mtundu wa anthu odziwikiratu wa iwo okha, (3) (3) Mulungu wa anthu a thupi la maonekedwe akutiakuti akutiakuti.

____5. Pa Yesaya 49:6 Mulungu ananena kuti chipulumutso chake chidzakhala cha (1) Dziko la Aisrayeli lokha, (2) Dziko la Afrika lokha, (3) Dziko lonse lapansi.

____6. Angelo ananena bwinobwino kwa abusa kuti Yesu ndiye Mpulumutsi wa anthu onse pa buku la (1) Mateyu 1:23, (2) Yohane 1:4-5, (3) Luka 2:10-11.

____7. Yohane Mbatizi ananena za Yesu kuti ndiye Mwanawankhosa amene akachotsa chimo (1) La Aisrayeli, (2) La dziko lapansi, (3) La anthu a ku Asia.

____8. Yesu Mzimu wake analamulira akuphunzira ake iwo ayenera kuphunzitsa (1) Anthu amitundu yonse, (2) Kuphunzitsa chimene Buku Lopatulika liphunzitsa, (3) Kuganiza bwino kwambiri.

____9. Anthu amene amanena kuti Yesu ali wamtundu umodzi okha wa anthu ali (1) Kulankhula bodza, (2) Kuphunzitsa chimene Buku Lopatulika liphunzitsa, (3) Kuganiza bwino kwambiri.

____10. Ngati akhristu amvera lamulo la Yesu, ayenera (1) Kukhala chete pa za Yesu, (2) Kuuza awo okha amene afuna za Yesu, (3) Kuuza ali yense za Yesu ndi za njira ya chipulumutso.



## KODI YESU NDANI?

DZINA______________________________ NAMBALA YA OPHUNZIRA__________

ADIRESI YANU______________________________________________

## MAYESO A PHUNZIRO 1

____1. Ndaphunzira ndime ya pamtima, Machitidwe 10:43, ndiponso ndanenanso kwa bwenzi langa (1) Inde. (2) Ayi.

____2. Ndawerenga madera onse a Mawu a Mulungu pa phunziro 1. (1) Inde, (2) Ayi.

____3. M'neneri Mika ananeneratu kuti Yesu adzabadwira mu (1) Yerusalemu. (2) Betelehemu, (3) Nazareti.

____4. Atate ake enieni a Yesu anali (1) Mulungu, (2) Yosefe, (3) Munthu wosadziwika.

____5. Yohane Mbatizi anazindikira Yesu chifukwa (1) Yesu anauza Yohane za Iye Mwini, (2) Yohane anaona zozizwitsa za Yesu, (3) Mzimu Woyera unadza nukhala pa Yesu.

____6. Yesaya ananeneratu kuti Yesu akanakhala (1) Munthu wosangalala , (2) Munthu wonyonzedwa ndi wokanidwa, (3) Wokongola kwambiri.

____7. Yesu anakwaniritsa uneneri wa Zakariya pamene analowa mu Yerusalemu. (1) Kuyenda ndi miyendo, (2) Atakhala pa mapewa a akuphunzira ake, (3) Atakwera pa bulu.

____8. Yudasi Iskariote anapereka Yesu chifukwa (1) Adani ake a Yesu anamuumiriza Yudasi, (2) Yudasi anafuna ndalama makumi atatu za siliva, (3) Mulungu anatero kuti Yudasi apereke Yesu.

____9. Kudanenedweratu kuti Yesu adzafa pamtanda chifukwa cha (1) Tchimo lake, (2) Kuopa kwa Pontio Pilato, (3) Machimo a anthu ambiri.

____10. Akuphunzira ake a Yesu sakanadabwa pa kuuka kwa akufa kwa Yesu ngati akadadziwa ndi kuzindikira, (1) Masalmo 16:10, (2) Deuterenomo 6:5, (3) Miyambo 28:13.

## MAYESO A PHUNZIRO 2

_____1. Ndaphunzira ndime ya pamtima, Mateyu 3:17, ndipo ndainenanso kwa bwenzi langa. (1) Inde, (2) Ayi.

_____2. Ndawerenga madera onse a mawu a Mulungu pa phunziro 2. (1) Inde, (2) Ayi.

_____3. M'ngelo anauza Yosefe kuti Yesu akanapulumutsa anthu ake ku (1) Umphawi, (2) Asilikali a Chiroma, (3) Machimo awo.

_____4. Mulungu Mwini wake anachitira umboni kuti Yesu anali (1) Mphunzitsi, (2) Mwana wa Iye yekha, (3) Wochita zozizwitsa wamphamvu.

_____5. Pamene mizimu yoipa inamzindikira Yesu kuti anali Mwana wa Mulungu, Yesu anaiuza iyo kuti (1) Ilape, (2) Ikhale chete, (3) Mukani lalikirani kwa anthu onse.

_____6. Petro anabvomereza kuti Yesu anali (1) Munthu wabwino kwambiri amene anali asanamuone ndi kale lomwe, (2) M'neneri, (3) Mwana wa Mulungu.

_____7. Pamene Yesu anafunsidwa kuti, "Kodi ndiwe Khristu, Mwana wa wolemekezeka?" Iye anayankha, (1) Ndine amene, (2) Sindine, (3) Kapena.

_____8. Ifenso tidziwa kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu chifukwa cha (1) Zobvala zake zokongola, (2) Kukondedwa kwake, (3) Kuuka kwake kwa akufa.

_____9. M'ngelo anauza Mariya kuti ufumu wa Yesu (1) Udzakhala wosatha, (2) Udzakhala zaka zambiri, (3) nthawi zonse udzakhala waung'ono.

_____10. Yesu ndi Mwana wa Mulungu chifukwa (1) anthu onse ali ana a Mulungu, (2) Mulungu ndiye Tate wake, (3) Anakonda Mulungu.



DZINA_____________________ NAMBALA YA OPHUNZIRA__________

ADIRESI YANU_____________________________________

## MAYESO A PHUNZIRO 11

_____1. Ndaphunzira mawu a pamtima Yohane 5:22, ndipo ndanenanso kwa bwenzi langa. (1) Inde, (2) Ayi.

_____2. Ndaphunzira mawu a Mulungu onse pa phunziro 11. (1) Inde, (2) Ayi.

_____3. Pa mawu a pamtima tiphunzira kuti anthu onse adzaweruzidwa ndi (1) Petro, (2) Atate, (3) Yesu, Mwana.

_____4. Chinthu chachikulu kwambiri choyenera kudziwa pa za chiweruzo, chilinkudza ndicho (1) Nthawi imene chidzakhala chiweruzo, (2) Ndani wina adzakhala kumeneko, (3) Tichikonzekera bwanji ife chiweruzocho.

_____5. Chiweruzo cha Yesu chidzakhala (1) Cholungama (2) Cholephera kudziwa machimo onse, (3) Chopanda chilungamo.

_____6. Makhalidwe athu a uzimu enieni aululikidwa ndi (1) Mawu athu, (2) Zochita zathu, (3) Kukhala kwathu kwa mumpingo.

_____7. Ngati munthu afuna kuti Yesu akamulandire pa tsiku la chiweruzo, iye ayenera (1) Kuuza anthu kuti Iye akhulupilire Mulungu, (2) Kulapa nalandira Yesu kuti ndiye Mpulumutsi, (3) Kusamala mkazi wake bwino.

_____8. Timaphunzira kuti munthu atayidwa kunja chifukwa cha machimo ake pa buku la (1) Machitidwe 9:20, (2) Aroma 6:23, (3) Machitidwe 16:31.

_____9. Timaphunzira kuti munthu akhala wokanidwa chifukwa (1) Akana kukhulupirira Yesu ndiye Mpulumutsi, (2) Amasuta fodya, (3) Analephera kulandira ubatizo

_____10. Malo a chilango chosatha achulidwa kuti nyanja ya moto pa buku la (1) Mateyu 25:46, (2) Mateyu 22:13, (3) Chibvumbulutso 20:14-15.

## MAYESO A PHUNZIRO 10

____1. Ndaphunzira mawu a pamtima, Machitidwe 2:36, ndipo ndanenanso kwa bwenzi langa, (1) Inde (2) Ayi.

____2. Ndawerenga mawu a Mulungu onse pa phunziro 10. (1) Inde, (2) Ayi.

____3. Yesu anafuna otsatira ake kuti azindikire (1) Kuti azikhala ofuna kumva zowawa. (2) Kuti nthawi zonse moyo wa Chikhristu ngwapafupi, (3) Kuti anthu ena onse adzakonda mkhristu.

____4. Pamene tinena kuti Yesu ali Ambuye wathu, titanthauza kuti (1) Tingathe kuchita zinthu monga tinga funire, (2) Yesu ali ndi ulamuliro onse pa ife, (3) Yesu ali bwenzi lathu.

____5. Yesu anaphunzitsa kuti munthu ayenera kuchita koposa kungovomeleza Ambuye ndi pakamwa poknapokha pa (1) Mateyu 20:28, (2) Mateyu 7:4, (3) Luka 16:10.

____6. Pamene Yesu ali Mbuye wathu, (1) Tidzakhla amanyazi kumubvomereza Iye pa maso pa anthu, (2) Tidzakhala chete ndi chikhulupiriro chathu, (3) Tidzamubvomereza pa maso pa anthu.

____7. Pamene Yesu ali Mbuye wathu, tiyenera (1) Kuchita monga tifuna ndi ndalama zathu, (2) Kugwiritsa ntchito ndalama monga mwa chifuniro cha Iye, (3) Kukhala osapereka ndalama zambiri ku ntchito za Mulungu.

____8. Timaphunzira zinthu za chifuniro cha Ambuye pabanja pa buku la (1) Aefeso 5:22, 6:4, (2) 1 Akorinto 10:13 (3) Yakobo 3:13-15.

____9. Pamene Yesu ali Mbuye wathu, (1) Tidzapemphera ku nyumba ya Mulungu pa Tsiku la Khrismasi lokha, (2) Tidzapemphera pokhapokha pamene taona mpata wabwino; (3) Tidzapemphera kawirikawiri.

____10. Pamene timvera Yesu monga Mbuye wathu, (1) Tidzauza anzathu za njira ya chipulumutso, (2) Tidzauza a mtundu wathu wokha za njira ya chipulumutso, (3) Tidzauza anthu onse za njira ya chipulumutso.



## KODI YESU NDANI?

DZINA____________________________NAMBALA YA OPHUNZIRA_____

ADIRESI YANU________________________________________

## MAYESO A PHUNZIRO 3

____1. Ndaphunzira ndime ya pamtima, Yohane 1:1, ndipo ndainenanso kwa bwenzi langa (1) Inde, (2) Ayi.

____2. Ndawerenga madera onse a mawu a Mulungu pa phunziro 3. (1) Inde, (2) Ayi.

____3. Pa mutu woyamba wa Yohane mawu onena kuti 'Mawu' atanthauza (1) Buku Lopatulika, (2) Mawu amene Mulungu analankhula, (3) Yesu.

____4. Mphamvu ya Yesu yokhululukira machimo itionetsa ife kuti Iye ndiye (1) Wokondeka, (2) Mulungu, (3) Munthu wodabwitsa.

____5. Timva kuti Yesu ayenera kulemekezedwa monga momwe Mulungu alemekezedwera pa (1) Yohane 3:16, (2) Yohane 5:23, (3) Yohane 10:27-28.

____6. Pamene Tomasi anapembedza Yesu monga Ambuye ndi Mulungu wake. Yesu (1) Anakana kumupembedza kumeneku, (2) Analandira kubvomerezedwa kwake ndi kupembedza kwake.

____7. Pa Afilipi 2:6 timva kuti Yesu sanabwere ku dziko lapansi (1) Monga Mulungu, (2) Wosanga ngati Mulungu kwenikweni, (3) Woposa Mulungu.

____8. Kodi ndi ndime iti imene itiphunzitsa kuti Ekelezia anagulidwa ndi mwazi wake wa Mulungu? (1) Yohane 14:6, (2) Machitidwe 20:28, (3) Machitidwe 10:43.

____9. Ndi mawu ati amene atiphunzitsa ife kuti Mulungu anali mwa Khristu? (1) Machitidwe 20:21, (2) Afilipi 2:10-11, (3) 2 Akorinto 5:19.

____10. Tidziwa kuti Mulungu ndi Yesu ali amodzi chifukwa ife (1) Tadziwa ndi nzeru zathu, (2) Taphunzira m'Buku Lopatulika, (3) Tauzidwa za chimenechi ndi olalikira.

## MAYESO A PHUNZIRO 4

____1. Ndaphunzira mawu a pamtima, Ahebri 4:15, ndipo ndanenanso kwa bwenzi langa, (1) Inde, (2) Ayi.

____2. Ndawerenga madera onse a Mawu a Mulungu pa phunziro 4. (1) Inde, (2) Ayi.

____3. Thupi la Yesu linali (1) Thupi la chilendo, la Uzimu (2) Thupi la m'nofu ndi magazi ngati matupi athu, (3) Thupi losamva kuwawa.

____4. Pamene Lazaro anafa, Yesu (1) Anaonerera nawo maliro ake, (2) Anatumiza kalata kwa Marita ndi Mariya, (3) Analira.

____5. Timaphunzira kuti Satana (1) Anayesa Yesu nthawi zambiri, (2) Sanamuyese Yesu kamodzi komwe, (3) Anamuyesa Yesu kamodzi kokha.

____6. Pa nthawi ina Satana adayesa kudzera mwa (1) Andreya, (2) Mfumu Herode, (3) Simoni Petro.

____7. Pamene Yesu adayesedwa Iye (1) Anapeputsa yeselo ndi mphamvu yake, (2) Nthawi zina anagonja nachimwa (3) Anakomana ndi mayeselo nawapambana.

____8. Mawu awa atiphunzitsa kuti Yesu anayesedwa koma sanachimwe (1) Aroma 6:23, (2) Aheberi 4:15, (3) Yesaya 53:6.

____9. Yesu anafa pamtanda (1) Chifukwa cha machimo athu, (2) Chifukwa analephera kuwathawa adani ake, (3) Chifukwa cha machimo ake Iye Mwini.

____10. Choonadi cha kuti Yesu anafa chifukwa cha machimo athu kuti tikhale wolungama kwa Mulungu mwa Iye chiphunzitsidwa pa (1) Yohane 5:24, (2) 2 Akorinto 5:21, (3) Yohane 1:12.



DZINA________________________NAMBALA YA OPHUNZIRA________

ADIRESI YANU______________________________________

## MAYESO A PHUNZIRO 9

____1. Ndaphunzira mawu a pamtima, Chibvumbulutso 1:18 ndipo ndanenanso kwa bwenzi langa (1) Inde, (2) Ayi.

____2. Ndawerenga mawu a Mulungu onse pa phunziro 9. (1) Inde, (2) Ayi.

____3. Mdani wa munthu amene analephereka kugonjetsedwa ndiye (1) Njobvu, (2) Umbuli, (3) Imfa.

____4. Pamene anali ndi moyo pa dziko lapansi, Yesu anaonetsa mphamvu yake yakupambana imfa pa (1) Kulankhula za imfa, (2) Kuukitsa iwo amene anali akufa, ( (3) Kusangalatsa ofedwawo.

____5. Yesu anadziwiratu zisanachitike kuti adzapachikidwa pamtanda. Iye ananena zimenezi pa (1) Mateyu 4:10, (2) Mateyu 10:37-39, (3) Mateyu 16:21.

____6. Yesu anachotsedwa pamtanda (1) Atakomoka, (2) Atafadi (3) Atayeseza kufa.

____7. Atauka kwa akufa, Yesu anaonekera kwa (1) Akuphunzira ake, (2) Wansembe wamkulu, (3) Asilikali amene anampachika Iye.

____8. Atauka kwa akufa, Yesu anaonekera kwa akuphunzira ake, (1) Kamodzi, (2) Kasanu ndi kawiri, (3) Nthawi zambiri.

____9. Kuuka kwa akufa kunaonetsa kuti Yesu anali (1) Munthu wabwino, (2) Mwana wa Mulungu, (3) M'neneri.

____10. Pa Yohane 5:28-29 timva kuti nthawi idzadza pamene Yesu (1) Adzaukitsa anthu onse abwino, (2) Adzaukitsa anthu onse ali m'manda, (3) Adzaukitsa anthu okhaokha amene ali ofunika.

## MAYESO A PHUNZIRO 8

____1. Ndaphunzira mawu a pamtima, Mateyu 1:21, ndipo ndanenanso kwa bwenzi langa. (1) Inde, (2) Ayi.

____2. Ndawerenga madera onse a mawu a Mulungu pa phunziro 8. (1) Inde, (2) Ayi.

____3. Pa Machitidwe 4:12 timva kuti (1) Anthu amipingo yonse adzapulumuka, (2) Okhaokha amene samva adzapulumuka, (3) Chipulumutso chiri mwa Yesu Khristu yekha.

____4. Yesu amatipulumutsa ife ku (1) Zobvuta zonse, (2) Chimo, (3) Umphawi.

____5. Timva kuti kuli malo a chilango chosatha kwa anthu osapulumuka pa (1) Akorinto 2:9, (2) Luka 16:19-31, (3) Aroma 12:1.

____6. Pamene munthu wapulumutsidwa, wapulumutsidwa ku (1) Chilango cha machimo, (2) Kupulukira, (3) Moyo wodwaladwala.

____7. Mkhristu akhoza kupambana uchimo chifukwa (1) Cha mphamvu yake, (2) Satana sadzamuyesanso, (2) Cha mphamvu ya Yesu imene ili mwa m'khristuyo.

____8. Timawerenga za ulemerero wa kumwamba pa (1) Yohane 3:18, (2) 1 Akorinto 4:1-2, (3) Mitu ya 21 ndi 22 ya Chibvumbulutso.

____9. Pamene munthu wasanduka m'khristu, Iye ali (1) wokhulupirira kuti adzakhala wolemera, (2) Cholengedwa chatsopano (ali ndi mtima watsopano), (3) Wokwiya nthawi zonse.

____10. Mkhristu ayenera kusunga thupi lake kulewa machimo chifukwa (1) Thupi lake liri Kachisi wa Mzimu Woyera, (2) Chimo lidzamudwalitsa, (3) Chimo lodzamuchititsa manyazi.



## KODI YESU NDANI?

DZINA ____________________ NAMBALA YA OPHUNZIRA ________

ADIRESI YANU ______________________________

## MAYESO A PHUNZIRO 5

____1. Ndaphunzira mawu a pamtima, Yohane 1:14, ndipo ndanenanso kwa bwenzi langa (1) Inde, (2) Ayi.

____2. Ndawerenga madera onse a mawu a Mulungu pa phunziro 5 (1) Inde, (2) Ayi.

____3. Pa Yohane 1:1-14 mawu onena kuti 'Mawu' atanthauza (1) Mawu amene Yesu adalankhula, (2) Yesu, (3) Buku Lopatulika.

____4. Aneneri a Chipangano Chakale ananena (1) Zinthu zonse zonena makhalidwe a Mulungu, (2) Sanena kanthu kali konse za Mulungu, (3) Choonadi chenicheni cha Mulungu koma osati choonadi chonse chonena za Iye.

____5. Mulungu sangazindikire bwino pokhapokha kuli kudzera mwa (1) Wolalikira wokhoza bwino, (2) Yesu Khristu, (3) Mpingo.

____6. Buku Lopatulika litiphunzitsa kuti (1) Pali njira imodzi yokha ya chipulumutso, (2) Pali njira zambiri za chipulumutso, (3) Anthu onse adzapulumutsidwa.

____7. Yesu aphunzitsa kuti chinthu chachikulu kwambiri kwa mkhristu ndicho (1) Mbiri yabwino, (2) Chifuniro cha Mulungu chifukwa cha moyo, (3) Chuma chambiri.

____8. Kuzindikira kwenikweni kwa moyo wamtsogolo itatha imfa kungachitike mwa (1) Pophunzira nzeru zozama za dziko, (2) Pomvera maganizo a anthu ena, (3) Kudzera mwa Yesu Khristu.

____9. Timaphunzira kuti Yesu ali chifanizo cha Mulungu pa Buku la (1) Chibvumbulutso 3:20, (2) Akolose 1:15, (3) Masalmo 14:1.

____10. Pa Chibvumbulutso 22:18-19 timva kuti Mulungu atsutsana ndi munthu amene (1) Aonjezapo kapena kuchotsapo pa mawu a Buku Lopatulika, (2) Wakuba, (3) Woledzera.

## MAYESO A PHUNZIRO 6

____1. Ndaphunzira mawu a pamtima, Mateyu 28:18, ndipo ndanenanso kwa bwenzi langa, (1) Inde, (2) Ayi.

____2. Ndawerenga madera onse a mawu a Mulungu pa phunziro 6. (1) Inde, (2) Ayi.

____3. Yesu anaonetsa mphamvu yake pakulamulira mphepo ndi nyanja pa (1) Masalmo 1:1, (2) Mateyu 8:23-27, (3) Yohane 14:2-3.

____4. Yesu anaonetsa mphamvu yake pa cholengedwa pa Mateyu 21:18-21 pa (1) Kulamulira mtengo wa mkuyu kuti uwume (2) Kutembenuza madzi kuti akhale vinyo, (3) Kudzetsa mvula.

____5. Tsiku ndi tsiku tiri kuloledwa kukhala ndi moyo pa dziko lino lapansi chifukwa cha (1) Mphamvu ya Satana, (2) Mphamvu yathu yathu, (3) Mphamvu ya Yesu Khristu.

____6. Ntchito ya Satana ndiyo (1) Kusangalatsa anthu, (2) Kuthandiza anthu, (3) Kuononga chimene chiri chabwino.

____7. Pamene mayi amene aononga ndalama zake zonse chifukwa chofuna kuchiritsidwa, anabwera kwa Yesu (1) Yesu anamukhululukira mayiyo chifukwa anali kupita kwa asing'anga, (2) Iye anamuchiritsa mayiyo, (3) Iye anakana kulankhula ndi mayiyo.

____8. Tiwerenga m'mene Yesu anachiritsira munthu wakhate pa (1) Marko 1:40-43, (2) Chibvumbulutso 3:20, (3) 2 Akorinto 5:17.

____9. Ngati munthu afuna chikhulukiro cha chimo, angathe kupeza chikhululukirochi (1) Mumpingo uli wonse, (2) Kudzera mwa ntchito zake zabwino, (3) Kudzera mwa Yesu Khristu yekha.

____10. Yesu anaonetsa mphamvu yake yopambana imfa, (1) Pakulankhula za imfayo, (2) Pakuukitsa akufa, (3) Pakuthawa imfa.



DZINA____________________NAMBALA YA OPHUNZIRA________

ADIRESI YANU______________________________

## MAYESO A PHUNZIRO 7

____1. Ndaphunzira mawu a pamtima, Yohane 1:29, ndipo ndanenanso kwa bwenzi langa. (1) Inde, (2) Ayi.

____2. Ndaphunzira madera onse a mawu a Mulungu pa phunziro 7. (1) Inde, (2) Ayi.

____3. Kodi ndani amene achulidwa Mwana wankhosa wa Mulungu mu Chipangano Chatsopano? (1) Yohane Mbatizi, (2) Yesu, (3) Mwana wankhosa woperekedwa nsembe ku kachisi.

____4. M'Chipangano Chakale kuperekedwa nsembe kwa mwana wankhosa chifukwa cha uchimo kunatiphunzitsa, kuti (1) Chimo liyenera kulangidwa ndi imfa, (2) Munthu angathe kuchita machimo monga m'mene angafunire, (3) Wansembe angathe kukhululukira chimo.

____5. Mulungu anafuna kuti Mwanawankhosa woperekedwa nsembeyo (1) Akhale wokalamba ndi wosafunika, (2) Akhale wabwinopo, (3) Akhale wopanda banga kapena chirema.

____6. Ndani anamuyesa Yesu kukhala ngati Mwanawankhosa wa Mulungu ndi kuti Iye analibe chimo? (1) Wansembe wamkulu, (2) Mose, (3) Mulungu.

____7. Yesu anali ngati Mwanawankhosa woperekedwa nsembe mu Chipangano Chakale chifukwa (1) Anaphedwa ndi mkulu wansembe wamkulu, (2) Anafera zochimwa za anthu ena, (3) Anali wosathandiza.

____8. Munthu asanalape ndipo asanalandire chikhulukiro ayenera (1) Kubatizidwa, (2) Kupita ku nyumba ya Mulungu, (3) Kuona kuchimwa kwake.

____9. Amosi 5:21-24, timva kuti Mulungu afuna (1) Kubvomereza machimo ako kwa wamsembe (2) Kulapa kwenikweni, (3) Kupereka nsembe yokha basi.

____10. Ngati munthu afuna chipulumutso cha Mulungu, ayenera (1) Kutsata chikonzedwe cha Mulungu cha chipulumutso, (2) Kupereka ndalama zambiri ku mpingo, (3) Kusamala munthu m'nzake bwinobwino.